# BOMA LATHU

*Kubweretsa Nkhani Mkhonde Lanu*

VOL. 46 NO. 7 | *YAULERE* | Boma Lathu, Julayi, 2024

# Zaka 60 zodzilamulira

WOLEMBA:
PRISCILLA PHIRI

MTSOGOLERI wa dziko lino, Dr Lazarus Chakwera, posachedwapa analamula kuti pachikondwerero cha ufulu odzilamulira chaka chino kukhale mwambo wamapemphero mu mzinda wa Lilongwe.

Chakwera ananena izi pamene dziko la Malawi likulirabe imfa ya amene anali wachiwiri kwa mtsogoleri wa dziko lino, Dr Saulos Chilima ndi Amalawi ena 8 omwe anatisiya pa ngozi ya ndege pa 10 Juni, 2024. Chaka chino, dziko la

TSAMBA 2



Wojambula: Nkhokwe yathu

*Dr Chakwera azatsogolera mapemphero a tsiku lokumbukira ufulu wadziko lino*

## Usi alumbiritsidwa kukhala wachiwiri kwa Pulezidenti

WOLEMBA:
MEMORY CHATONDA

WACHIWIRI kwa Mtsogoleri wa dziko lino watsopano, Dr. Michael Bizwick Usi, walonjeza kuti agwira ntchito modzipereka kuti akwaniritse cholinga cha Mtsogoleri wa dziko lino, chofuna kutukula miyoyo ya Amalawi.

A Usi ananena izi atasankhidwa ndi Mtsogoleri wa dziko lino Dr. Lazarus Chakwera, posachedwapa kukhala wachiwiri wawo, potsatira imfa ya malemu Dr. Saulos Chilima pa ngozi ya ndege yomwe inachotsanso miyoyo ya anthu ena asanu ndi atatu.

A Usi, omwe amagwira ntchito ngati wachiwiri kwa mtsogoleri wa chipani cha UTM komanso Nduna ya zachilengedwe komanso yowona za kusintha kwa nyengo, analumbiritsidwa ku nyumba ya Malamulo mu nzinda wa Lilongwe.

Polankhula atalumbiritsidwa pa Udindowu, a Usi anati iwo ndiwokonzeka

TSAMBA 3



**Malawi, Israel akhwimitsa mgwirizano olemba anthu ntchito kunja**

TSAMBA 3



**Anyezi ndi opindulitsa kwambiri**

TSAMBA 5



**GESD ilimbikitsa atsikana pomanga zipinda zogona mmasukulu**

TSAMBA 11

## Ndemanga

### Tikondwerere moganizira amene anatisiya

Posachedwapa dziko lino linali pachisoni chachikulu pamene tinataya miyoyo ya wachiwiri kwa Mtsogoleri wadziko lino, Dr Saulos Klaus Chilima, ndi ena ogwira nawo ntchito asanu ndi atatu.

Imfayi inadza pamene dziko lino limayembekedzera kukwanitsa zaka 60 za ufulu odzilamulira kuchokera mmanja mwa asamunda, pa 6 Julaye chaka chino.

Powona kuphatikizana kwa chisonichi ndi chisangalalo cha ufulu wadziko lathuku, Boma lawona kuti chisangalalo chachaka chino chikhale munjira ya mapemphero.

Ganizoli lomwe Mtsogoleri wadziko lino anapereka ndilotamandika kwambiri poganizira kuti kukanakhala kusowa umunthu kusangalala pomwe misozi yathu idakali kutsika mmasaya athu chifukwa cha imfa za Amalawi omwe anatisiyiwa.

Pamene Boma lakhazikitsa mapemphero otere panthawiyi, tiyeni nafe Amalawi tichite chimodzimodzi kumadera athu, kupempherera mizimu ya anzathuwa munyengoyi powonetsa umodzi wathu.

Pamene takwanitsa zaka 60 za ufulu ozilamulira ndi nthawinso yoti ife eni Amalawi tiwunike komwe tachokera ndikuyang'ana patsogolo pachitukuko cha miyoyo yathu komanso dziko lathu. Chitukuko chadziko sichibwera ndi Boma lokha ayi koma chimayambira pakhomo lomwe tikuchokera ndipo kenako ndikuyamba kuthandiza Boma pandondomeko zake zachitukuko.

Tikagwira ntchito limodzi moyang'ana patsogolo dziko lathu lizatukuka ndikunyadira zomwe takwanilitsa pokumbukira tsiku la ufulu wathu mzaka zikubwerazi.

Ife a Boma Lathu tikuthokoza mtsogoleri wadziko lino potsogolera dzikoli mwaluntha ndikuliwunikira pazambiri kuphatikizapo kuyika mapemphero pachisangalalo cha ufulu wathu chaka chino

# Achinyamata ali ndikuthekera kokweza chuma- Chakwera




Wojambula: Govati Nyirenda

*Dr Lazarus Chakwera kucheza ndi achinyamata kunyumba ya chifumu*

WOLEMBA
SELLAH SINGINI

Mtsogoleri wa dziko lino Dr. Lazarus Chakwera wati achinyamata ali ndikuthekera kokweza ntchito zachuma chadziko lino.

Achakwera analankhula izi pamwambo olandira atsogoleri achinyamata ochokera m'madera osiyanasiyana adziko lino kunyumba ya boma ya Kamuzu ku Lilongwe.

Iwo anati achinyamata ali ndi luntha lopanga zambiri potukula chuma komanso ulimi, zokopa alendo ndi migodi, chifukwa cha khama lawo, malingaliro awo, kulimbikira kwawo komanso chidwi chawo chofuna kusintha zinthu mdziko.

"Ndichifukwa chake ndikukulandirani inu atsogoleri omwe muli ndikuthekera kosintha zinthu. Ndafuna ndikuthokozeni chifukwa chomvetsetsa kuti ino ndi nthawi yanu yowunikira maluso anu ngati nyali pamdima wa mavuto omwe tikukumana nawo. Zikomo chifukwa chomvetsetsa kuti ili ndi boma lanu loyendetsedwa molingalira inu.

"Kumbukirani kuti ndinu chuma chamtengo wapatali, osati katundu wolemera. Kukhala wachinyamata ndi mwayi, osati cholepheretsa. Kukhala wachinyamata ndi mphamvu, osati vuto," anatero a Chakwera.

Iwo analimbikitsa achinyamata kuti asalole wina aliyense kuwanyoza chifukwa choti iwo ndi achinyamata.

Nduna ya Achinyamata ndi Zamasewero, Uchizi Mkandawire, anayamikira a Chakwera chifukwa chopeza mpata tsiku lonse kucheza ndi achinyamata ponena kuti uwu ndi umboni wakuti mtima wawo umakhala pa achinyamata.

Mkandawire anati msonkhano umene Mtsogoleriyu anali nawo ndi otsogolera achinyamata wo unapereka mphamvu kwa achinyamata yobwerera ku madera awo ndi kuyamba kugwira ntchito zambiri pothandiza kutukula dziko.

"Nditsimikizire kuti ndalama ndi nthawi zomwe mwagwiritsa ntchito polandira ndi kulimbikitsa achinyamatawa sizidzidapite pachabe. Lero mwadzala mbewu zomwe zizathandiza kubala zipatso. Pasanapite nthawi mudzaitanidwa kuti mukawone zipatso zomwe zidzakhalapo chifukwa cha msonkhanowu," anatero Mkandawire.

Pamwambowu achinyamata anasangalala ndi nyimbo zoyimbidwa mwaluso ndi wachinyamata nzawo Eli Njuchi komanso Gulu loyimba la Apolisi.

# Chikondwerero chikhala chamapemphero

YACHOKERA PA TSAMBA 1

Malawi lakwanitsa zaka 60 chitengereni ufulu wake kwa atsamunda pa 6 Julaye, mchaka cha 1964. Mwachizolowezi, tsikuli limakumbukiridwa ndi chikondwerero pamene Amalawi motsogozedwa ndi mtsogoleri wa dziko lino amasonkhana ndi kusangalala pamodzi ndizochitika zosiyanasiyana monga magule, perete wa asilikali, nyimbo, masewero ampira wamiyendo mwa zina. Koma chaka chino pamene dziko la Malawi lataya yemwe anali mtsogoleri wachiwiri wa dziko lino, boma linaganiza kuti tsikuli lisakumbukiridwe mwa zaka zonse koma mmalo mwake kukhale mwambo wa mapemphero popeza dzikoli likanali pachisoni. Poyankhula ku mkumano wa atolankhani, mneneri wa boma yemwenso ali Nduna ya Zofalitsa Nkhani, a Moses Kunkuyu, posachedwapa anati chisangalaro chimene chimachitika pa tsikuli, chaka chino sichikhalapo ngakhale nthawi yokhuza ikhale itatha.

"Mtsogoleri wa dziko lino wanena izi chifukwa tikanali pa chisoni potsatira imfa ya a Chilima ndi Amalawi ena 8 omwe anatisiya pa ngozi ya ndege," anatero a Kunkuyu. Amene amayankhulapo pankhani za ulamuliro wabwino, a Wonderful Mkutche, anati maganizo oti chikondwerero cha chaka chino chichitike mwakachetechete ndi abwino kwambiri.

"Dziko lathu liri pa maliro kotero kuti sipakuyenera kuchitika chikondwerero chiri chonse pa nthawiyi," anatero polankhula. Chikondwerero cha ufulu odzilamulira wachaka chino, umayembekezeka kuchitikira mu mzinda wa Blantyre motsogozedwa ndi mtsogoleri wa dziko lino.

# Usi alonjeza kudzipereka kutumikira mtundu wa Amalawi

YACHOKERA PA TSAMBA 1

kugwira ntchito mozipereka pa udindo wa wachiwiri kwa mtsogoleri wa dziko lino pothandiza kutukula dziko lino.

"Anthu ena atha kuganiza kuti kusankhidwa kukhala wachiwiri kwa mtsogoleri wa dziko lino ndizikhala moyo osangalala. Zoona zake ndizakuti, palibe chisangalalo muzinthu zonsezi, chifukwa ndi nsembe yomwe ndi ntchito yotumikira anthu.

"Ngati wachiwiri wa Mtsogoleri wa dziko, sindiziganiziranso za moyo wanga kapena za banja langa, koma ndiyenera kukhala ngati gogo amene amangoganizira zofuna za ana ake ndi zidzukulu zake nthawi zonse, umene uli utumiki wapadera," anatero a Usi.

Iwo anawonetseranso chisoni chachikulu pa imfa ya a Chilima ndi kuwathokoza pokhala munthu oyamba kuwakhulupirira powatenga kukhala wachiwiri wawo.

A Usi analonjeza kudzipereka kutumikira mtundu wa Amalawi ndikulemekeza mzimu wa a Chilima pogwira ntchito molimbika.

"Pamene ndikulumbira, ndikukulonjezani kuti ndidzipereka nsembe ku dziko la Malawi, nzika zake, ndi mbendera yake, chifukwa iyi ndi njira yabwino yolemekezera malemu Dr. Saulos Klaus Chilima," anatero polankhula.

A Usi anatenganso nthawi kuyamikira a Chakwera chifukwa chokhala mzati wa mphamvu pamene Amalawi amalira maliro a malemu Chilima.

Mwambo olumbiritsa wachiwiri kwa mtsogoleri wa dziko linowu, unasonkhanitsa pamodzi akuluakulu aboma motsogozedwa ndi Mtsogoleri wa dziko lino, Dr. Lazarus McCarthy Chakwera. Mwa ena omwe analipo pamwambowu ndi sipikala wa nyumba ya malamulo olemekezeka a Catherine Gotani Hara, aphungu a nyumba ya Malamulo, Nduna za boma, akuluakulu oweruza milandu ndi Amalawi ochokera mmadera osiyanasiyana mdziko lino .



Wachiwiri kwa Mstogoleri wadziko lino, a Michael Usi kulumbira

# Malawi, Israel akhwimitsa mgwirizano olemba anthu ntchito

WOLEMBA
ROBERT KATULI

MABUNGWE olemba anthu ntchito omwe siaboma, sazitenganso nawo gawo pantchito yolemba Amalawi omwe akuyembekezeka kukagwira ntchito ku Israel popeza boma la Malawi ndi lokhalo limene likhale likugwira ntchitoyi.

Nduna yowona za Antchito, a Agnes NyaLonje, ananena izi posachedwapa, mu mzinda wa Lilongwe pamwambo wa atolankhani odziwitsa anthu za momwe dongosolo la ogwira ntchito ku dziko la Israel likuyendera pakadalipano.

A NyaLonje anati izi zikutsatira mgwirizano wa maboma awiriwa, okhudza anthu okagwira ntchito kunja umene boma la Malawi ndi boma la dziko la Israel linasayinira pa 18 Epulo chaka chino.

"Cholinga cha mgwirizanowu ndi kulimbikitsa chitetedzo cha maufulu a anthu ogwira ntchito, thanzi ndi umoyo wa anthu ogwira ntchito akuno ku Malawi mdziko la Israel, kuti asalembedwe ntchito ndi mabungwe ena akapita uko komanso panthawi yomwe akugwira ntchito mpaka kubwerera ku Malawi.

"Maufulu wa adzatetedzedwanso chifukwa cha kupezeka kwa ofesi ya kazembe wa dziko la Malawi yomwe idakhazikitsidwa ku Israel komwe anayikanso munthu wogwira ntchito mu undunawu," anatero A NyaLonje.

Iwo anatinso mabungwe olemba anthu ntchito omwe si a boma a mdziko muno analoledwa kulemba anthu ogwira ntchito kuti akagwire ntchito mongoyembekezera m'gawo la ulimi ku Israel kuyambira mwezi wa Disembala 2023 mpaka Januware 2024, yomwe inali nthawi yolemba anthu ntchito mwaganyu.

Iwo anaonjezera kuti, pamene nthawi yolembera anthu ntchito mwaganyu inatha, nthawi ya mabungwe olemba anthu ntchito amdziko muno omwe si aboma, inatsekedwanso potsatira Malamulo.

"Komabe, boma lawona kuti mabungwewa anapitirirabe kulemba anthu ntchito nthawi ya pa 31 Januwale 2024, yomwe inakazikitsidwa ndi dziko Israel itatha.



Agnes NyaLonje, Nduna yowona za Antchito

Izi zapangitsa kuti achinyamata ena azidikirabe ulendo opita ku dziko la Israel," inatero Ndunayi.

Iwo ananenanso kuti ntchito yatsopanoyi ikangoyambika, boma liganiziranso achinyamata omwe analembedwa ntchito ndi mabungwewa nthawi yolembera anthu ntchito imene idakhazikitsidwa ndi dziko la Israel, itatha.

A NyaLonje anatinso pali zikalata zoonjezera zitatu zomwe maboma awiriwa akuyenera kumalizitsa unduna wawo usanayambe kulemba anthu ntchito.

"Mkumano wapakati pa Malawi ndi akatswiri a mdziko la Israel unakonzedwa kuchitika pa 5 Juni 2024 kuti amalizitse zikalata zoonjezera zomwe ziri pamwambazi," anatero.

Mwa zina, pokonzekera kutumiza anthu ogwira ntchito ku Israel, Unduna wa Zantchito uyamba kukambirana ndi oyang'anira zantchito mmaboma, ogwira ntchito ya zaumoyo, oyang'anira zolowa ndi kutuluka komanso apolisi pa ndondomeko yonse yolembera anthu ntchito komanso ntchito yomwe aliyense adzagwire.

Mlembi owona za ntchito, a Chikondano Mussa, anati ukadaulo okhudza zotumiza anthu ogwira ntchito kunja, uperekedwa ndi bungwe la mgwirizano wa mayiko amu Africa pa nthawi ya ntchitoyi.

Mgwirizano omwe mayiko awiriwa anasayinirana unakhazikika pa kulemekezana, komanso kudzipereka pofuna kulimbikitsa chitukuko cha chikhalidwe cha anthu komanso mbali ya zachuma.

Pamapeto ake, dziko la Malawi likhala likupanga mgwirizano wolimba ndi dziko la Israeli.

# Mlatho wa Lifani wathetsa mavuto


ZA UMOYO
Wojambula: khokwe yathu

*Mlatho wa Lifani m'boma la Zomba*

WOLEMBA
MARTIN CHIWANDA

PATUMA anabadwira mmphepete mwa mtsinje wa Lifani mchaka cha 1995 pomwe mayi ake, Edna Saizi ankadikira kuti madzi mumtsinjewu aphwe kuti awoloke kukachilira pa chipatala chaching'ono cha Machinjiri m'boma la Zomba.

Saizi anati Mtsinjewu uli ndi mbiri yaikulu kubanja lawo pomwe anabadwitsa mwana wawo oyamba pamtsinjewu pomwe mitengo yomwe inasanjikidwa pamtsinjewu ngati powolokera inali itakokoloka ndi madzi mchaka cha 1994.

"Mtsinje wa Lifani uli ndi mbiri yosaiwalika m'banja mwanga. Ndinaberekera pamtsinje umenewu titalephera kuwoloka matenda atayamba. Zinali zovuta koma panalibe kuchitira mwina, mwamwayi ndidabereka mwana bwino lomwe. Mwanayu akanakhala wamwamuna, ndikanatha kumpatsa dzina loti Lifani kuti dzinali likhalebe mmbiri ya moyo wabanja langa," adatero a Saizi Matache ochokera mmudzi wa Matache, Mfumu yaikulu Mposa ku Machinga.

Si banja la a Saizi lokha lomwe liri ndi nkhani pamtsinjewu, anthu ambiri ammidzi yozungulira mtsinjewu, akhala akukumana ndi mavuto osinayasiyana chifukwa chakusowa kwa mlatho pantsinjewu.

Mtsinje wa Lifani wakhala chipsinjo chomwe chimalepheretsa anthu kufikira zofunikira zambiri pamoyo wawo monga zipatala, sukulu komanso zitukuko zina.

"Kukangogwa mvula ndekuti ife tatsekeredwa. Kupatula kuvutika kupeza thandizo la chipatala, ana a sukulunso amalephera kuoloka ndipo miyoyo ina idatayikapo pamtsinje umenewu," adatero a Saizi.

Koma ngakhale zinali chomwechi, zonsezi lero ndi mbiri chabe kutsatira mlatho wamakono omwe wamangidwa pa tsinjewu ndithandizo la ndalama lochokera kuntchito yolimbikisa ulamuliro wabwino pachitukuko ya Governance to Enable Service Delivery (GESD).

A Saizi anayamika boma poganizira zomanga mlatho wa Lifani ponena kuti upulumutsa anthu wochuluka komanso kulimbikitsa ntchito zachitukuko mderali.

Nawo a Aubrey Jaya, anavomerezana ndi a Saizi ponena kuti anthu amavutika kwambiri pa mtsinjewu makamaka nthawi yamvula ngakhalenso ana a sukulu chifukwa mtsinjewu ndi waukulu ndipo umatenga madzi ochuluka.

"Ngakhale ma bizinesi athu samayenda moti chuma cha anthu chimalowa pansi nthawi zambiri. Mtsinje umenewu unali ngati malire pazokhumba zawanthu chifukwa kuti anthu apite kuchipatala sikunali kophweka. Anthu amalephera kuoloka mtsinjewu zomwe zimaphera anthu ufulu wachithandizo chazaumoyo.

"Koma lero tikuyamika GESD chifukwa chantchito yopambana yomwe yathetsa mavuto a anthu pamayendedwe ku dera lino ndipo pano ndife okondwa kwambiri," adatero a Jaya,

Poonjezerapo a Happiness Dinesi anati amayi tsopano ali ndismwayi opita ku sikelo nthawi iliyonse akakhala oyembekezera ndipo kuti mavuto oberekera panjira athetsedwa ndi kumangidwa kwa mlatho wa Lifani.

"Tikuthokoza boma chifukwa chotiganizira kudera lino. Ana tsopano akupita ku sukulu mosavuta ndipo sakusiyira panjira maphunziro ngati kale pamene amalephera kuoloka mtsinjewu,"

Mfumu yaikulu Mposa inayamika boma chifukwa cha mlathowu ponena kuti anthu ambiri mdera lake athandizika atavutika kwanthawi yaitali ndi mtsinjewu.

BOMA LATHU Nyuzipepala

**Mlangizi**
William malimero

**Mkonzi**
Daniel Kasondo

**Dizayinala wamkulu**
Eugene Makwakwa

**Dizayinala wachiwiri**
Annie Kakolo

Nyuzipepalayi imafalitsidwa ndi Unduna wa Zofalitsa nkhani

*P/Bag 310, Capital City, LL3*
***www.ict.gov.mw***

*Boma Lathu nyuzipepala inakhazikitsidwa ndicholinga chophunzitsa ndi kudziwitsa mtundu wa Amalawi popititsa patsogolo ntchito zachitukuko.*

# Alimi alandira mapampu amadzi oyendera mphamvu ya dzuwa

ZA ULIMI



*Tikufuna kulimbikitsa ulimi - Bulukutu*

WOLEMBA
GEORGE MPONDA

PAMENE Boma liri ndi udindo pachitukuko chadziko, mabungwe omwe si a boma samangokhala, nawo amatenga mbali pantchito zosiyanasiyana zotukula dziko lino.

Posachedwapa, bungwe la Catholic Development Commission (CADECOM) kudzera mu ntchito zachitukuko za dayosizi ya Karonga, lati lithandiza alimi 450 a m'dera la Mfumu yaikulu Wasambo m'chigawo chakumpoto, powapatsa mapampu opopera madzi makumi atatu oyendera mphamvu ya dzuwa.

Mkulu wantchitoyi m'bungwe la CADECOM, a Mathias Bulukutu ananena izi m'boma la Chitipa pokhazikitsa ntchito ya zaka ziwiri yotchedwa 'Climate Justice Communities' (CJC).

Iwo anati, "Ntchitoyi ikufuna kupereka mphamvu kwa anthu kuti ayike zofuna zawo mundondomeko yachitukuko chomwe akufuna kuti zithe kukwaniritsidwa kudzera mu ntchitoyi,

"Mwa zina, tikufuna kulimbikitsa ulimi pokhazikitsa ndondomeko zosiyanasiyana zoti zipindulire miyoyo ya anthu," anatero a Bulukutu.

Mkulu owona za ulimi wamthirira m'boma la Karonga, a George Chanya, adati mavuto omwe amabwera chifukwa cha kusintha kwa nyengo padziko lonse lapansi asokonezanso ntchito zaulimi kuno ku Malawi.

"Kuti alimi adzidyetse okha ngakhale kugulitsa zokolola zawo pamene akulimbana ndi mavuto akusintha kwa nyengo, ntchito zaulimi ziyenera kukhala zoyenera motsatana ndinyengo. Zosowa monga madzi ndi nthaka ziyenera kugwiritsidwa ntchito bwino kuti alimi azitha kukolola zambiri atalowetsa zochepa.

"Kupereka mapampu a madzi oyendera mphamvu ya dzuwa kwa alimi kuwathandiza kulimbikitsa ulimi potero zipititsa patsogolo kapezedwe ka chakudya m'dziko muno" iwo sanaonjeza.

Ntchitoyi ikuthandizidwa ndi thumba la Climate Justice lochokera ku Boma la Scotland

# Anyezi ndi opindulitsa kwambiri

WOLEMBA
HASTINGS YOBE

ANYEZI ndi mbewu imodzi imene imabweretsa ndalama zochuluka kwa alimi mdziko lino. Anyezi wambiri mdziko muno amalimidwa ndi alimi ang'onoang'ono.

Malinga ndi kafukufuku yemwe anachitika mchaka cha 2020, dziko la Malawi linatumiza matani opitilira 10,000 a anyezi ku Zambia kokha, zomwe zinapezetsa dziko lino ndalama zochuluka.

Ulimi wa anyezi umapereka phindu lochuluka kwa alimi ang'onoang'ono mdziko muno chifukwa ulimiwu sumafuna zambiri, izi zimapangitsa ulimiwu kukhala odalirika pakati pa alimi ambiri maka akumidzi.

Ubwino wina wa ulimiwu ndi osavuta kulima ndipo amafuna ntchito ndi madzi ochepa poyerekeza ndi mbewu zina.

Komanso anyezi sagwidwa ndi tizirombo komanso matenda, izi zimathandiza kuchepetsa kufunika kwa mankhwala ophera tizirombo ndi mankhwala ena.

Mbewuyi, imatha kusungidwa kwa nthawi yayitali, zomwe zimapereka mpata kwa alimi kusunga mbewuyi mpaka mitengo itafika pabwino mmisika.

Blessings Mlelemba ndi mmodzi mwa alimi omwe akhala akuchita bwino ndi ulimi wa anyezi ku Lunzu m'boma la Blantyre.

Mlimiyu akuyembekeza kupeza ndalama zosachepera K4 miliyoni kuchokera mu zokolola zake za anyezi chaka chino.

"Chaka chino ndikuyembekezera kupeza K4 miliyoni nditagulitsa anyezi wanga yemwe ndinakolola pa munda wanga wa theka la ekala," Mlelemba anatero.

Mlimi wina wa ku Zomba, Gavily Maluwa, ndi mmodzi mwa alimi amene amagwiritsa ntchito luso lomwe anapeza ku sukulu ya ukachenjede ya Lilongwe University of Agriculture and Natural Resources (LUANAR) kuti apeze phindu lalikulu, ndipo amapeza ndalama zokwana K900,000 kuchokera ku malonda ake a anyezi.

"Nthawi zina, ndimatulutsa Anyezi wa ndalama zokwana K900,000, koma zimatengera amene akugula anyezi, mwachitsanzo ngati munthu akugulitsa anyezi m'mahotela kapena m'malesitilanti ndi pamene mitengo ya anyezi imakhala yokwera," anatero Maluwa.



*Ulimi wa anyezi ndiwopindulitsa kwambiri*

Iye anawonjeza kuti, "Anyezi sawononga ndalama zambiri polima poyerekezera ndi phindu limene mlimi amalipeza atagulitsa anyeziwu, mwachitsanzo anyezi safuna kugwiritsa ntchito mankhwala ophera tizirombo kapena feteleza wambiri koma ndi chisamaliro chabwino chokha mlimi akhoza kupeza zokolola zambiri."

Iye amakhulupirira kuti ngati boma lingayikepo chidwi pa ulimi wa anyezi lingathandize kuthana ndi vuto la kusowa kwa ndalama yakunja mdziko muno.

Katswiri wa ulimi wa ndiwo za masamba za mmadimba ku sukulu ya ukachenjede ya za ulimi ya LUANAR Bunda Campus, Dr. Vincent Mwale anavomereza kuti ulimi wa anyezi ndi wopindulitsa chifukwa kulima kwake ndi kosavuta, ntchito imakhala yochepa, komanso kulimbana ndi tizirombo ndi matenda kumakhala kochepa.

Iye analimbikitsa alimi kudzala mbewu yamitundu ya Texas Grano ndi Red Creole, yomwe imagwirizana bwino ndi nyengo ya kuno ku Malawi komanso imayenda malonda mmisika yambiri.

# Kukondwerera zaka makumi asanu ndi chimodzi za chitukuko cha zaumoyo

WOLEMBA
PRISCILLA PHIRI

Mu mndandanda wa zitukuko zomwe zachitika mzaka makumi asanu ndi chimodzi mdziko muno, nthambi ya zaumoyo mdziko muno yachita zitukuko zambiri ndipo yakhala bwenzi losatopa la anthu komanso chiyembekezo chodalirika cha tsogolo la umoyo wa anthu.

Ngakhale mzakazi munali mavuto a zachuma, kusowekera kwa zipangizo mzipatala, kuperewera kwa ogwira ntchito, miliri ndi zovuta zina zokhudzana ndi kusintha kwa nyengo, azaumoyo mdziko muno anagwira ntchito molimbika pothandiza anthu munjira zosiyanasiyana.

pamene dziko lino likukondwerera zaka 60 zodziyimira pa lokha chaka chino, anthu sakusangalala chifukwa cha ufulu okha koma akukumbukiranso zomwe dziko lakwanitsa komanso mavuto omwe dziko ladutsamo kufikira chaka chino.

Mzaka zoyambirira titalandira ufulu, dziko lino linali ndi zipatala zochepa. Boma linali ndincthito yayikulu yomanga zipatala chifukwa chipatala chachikulu chinali chimodzi chokha chomwe ndi cha Queen Elizabeth ku Blantyre chimene chinatsegulidwa mchaka cha 1959.

Kunali kofunika kwambiri kuti zipatala zambiri zimangidwe mdziko muno, kotero kuti boma lidaganiza zoyamba kutsegula zipatala mmabona ndi zing'onozing'ono mmidzi.



Hallima Daud, wachiwiri kwa Nduna yaza Umoyo



Boma liyike ndalama zambiri ku za Umoyo - Jobe

Zipatalazi zidali maziko a ndondomeko ya zaumoyo ya dziko lino, pamene anthu akumidzi anayamba kulandira thandizo loyenera pothana ndi matenda osiyanasiyana monga malungo komanso chifuwa cha chikulu (TB).

Mzaka zino Boma linawona kuti ndi kofunika kwambiri kuti likhale ndi ndondomeko zokhazikika polimbikitsa zaumoyo pochita maubale ndi mabungwe komanso maiko ena othandiza pantchito za umoyo.

Kwa zaka zambiri, kukhazikitsa zipatala chakhala chinthu chofunikira kwambiri. Kudzipereka kwa boma pochulukitsa zipatala kwathandiza dziko lino kukhala ndi zipatala zochuluka mmadera onse adziko lino.

Boma pansi pa utsogoleri wa Dr Lazarus McCarthy Chakwera, wayika chidwi chomanga zipatala za mmadera mazana asanu ndi anayi (900) ndi cholinga chofuna kuwonetsetsa kuti Amalawi akukhala ndi zipatala pafupi monga chimodzi mwa masomphenya a bungwe lowona za umoyo la dziko lonse lapansi la World Health Organization (WHO).

Mchaka cha 2023 wachiwiri kwa Nduna ya za Umoyo, Halima Daudi, analengeza kuyamba kwa ntchito yomanga zipatalazi pa tsiku lokondwerera kupezeka kwa zipatala ponseponse.

Iwo anati gawo loyamba la ntchitoyi, munali kumanga kwa zipatala 55 zimene 20 mwa izo zidamalizidwa kale.


Chipatala cha Queens mu nzinda wa Bslantyre

Potukula za Umoyo, Boma linachulukitsa chiwerengero cha ogwira ntchito mu Unduna wa za umoyo polemba wogwira ntchito 1,246 kuti apititse patsogolo umoyo wabwino mdziko muno.

Mzaka makumi asanu ndi chimodzi dziko lino lakhala likukumana ndi mavuto ambiri amatenda opatsirana ndi osapatsirana monga Edzi, TB, khate, malungo, Kolera komanso Covid-19. Ndipo Unduna wa za Umoyo unakhazikitsa ndondomeko komanso ntchito zolimbana ndi mtundu uliwonse wamatenda mdziko muno.

Kudzera mu ndondomeko zimene boma lidakhazikitsa monga kupereka mankhwala wotalikitsa moyo, katemera komanso kufalitsa mauthenga azaumoyo kunachepetsa chiwerengero cha anthu amene amafa ndi edzi, Covid-19, TB ndi matenda ena.

Mlembi wamkulu mu Unduna wa za umoyo, Dr Martias Joshua, anati chiwerengero cha imfa zobwera chifukwa cha matenda a Chifuwa chachikulu cha TB komanso Khate chatsika kwambiri.

Masomphenya a bungwe la za umoyo pa dziko lonse lapansi la World Health Organisation ndi owonetsetsa kuti aliyense mosatengera chuma kapena kumene akupezeka azikhala ndi mwayi wogwiritsa ntchito zipatala.

Mogwirizana ndi masomphenyawa, boma la Malawi linayamba kuyika ndalama zochuluka ku ntchito zaumoyo kuti a Malawi azilandira thandizo la ulele. Kafukufuku, wawonetsa kuti dziko lino liri ndi tsogolo lowala la umoyo wabwino zomwe ndi zosiyana ndi mayiko ena omwe nawo ali osauka.

Mkulu wabungwe lowona zamgwirizano pankhani za Umoyo la Malawi Healthy Equity Network, a George Jobe anati kukwera kwa chiwerengero cha anthu mdziko muno kumabweretsa mavuto a zaumoyo komanso kupangitsa kuti ogwira ntchito ya chipatala akhale woperewera.

“Tikumanabe ndi mavuto akusowekera kwa mankhwala ena, kuchepa kwa ogwira ntchito mzipatala, komanso kuchepa kwa magalimoto onyamulira odwala.

"Tikuyenera kuyika ndalama zambiri ku za umoyo,” anatero a Jobe.

Pamene tikukondwerera zaka 60 za ufulu odzilamulira zaonetsa kuti ntchito za umoyo zikupita patsogolo. Ulendo okwaniritsa kuti aliyense azikhala ndi mwayi ogwiritsa ntchito chipatala uli mkati, ndipo Boma ndi abwenzi ena adzipereka kotheratu kutukula miyoyo ya Amalawi.

# Kuthetsa mavuto a madzi ndi sikimu ya Tsamba

WOLEMBA
LEAH MALIMBASA

KWA zaka zambiri, anthu a m'mudzi wa Tsamba, mdera la Mfumu yaikulu Ngabu, m'boma la Chikwawa, akhala akuvutika ndi kusowa kwa madzi. Vutoli limapangitsa amayi Selena Ganizani ndi ena kuyenda mtunda wa makilomita anayi, pofuna kupeza madzi oti agwiritse ntchito m'nyumba zawo.

Akafika kumtsinje wa Phwadzi, amapeza mizere italiitali ya anthu odikira kutunga madzi.

"Vuto limeneri linakhudzanso mabanja athu chifukwa limapangitsa kuti amuna ena azitikayikira, zomwe zimasokoneza mgwirizano wa m'mabanja," anatero Mayi Ganizani.

Mchaka cha 2009, bungwe la Water for People, lomwe silaboma, linayamba kugwira ntchito mderali.

Malingana ndi Mkulu wantchitoyi m'bungwe la Water for People m'boma la Chikwawa, a Israel Mtegha, anati ntchitoyi inali yopereka madzi a ukhondo kwa anthu akumidzi ngakhale kuti m'mbuyomu ntchitoyi inakumana ndi mavuto akupezeka kwa mchere mmadziwo.

"Mchaka cha 2017, mothandizidwa ndi ndalama zochokera ku boma la Scotland, komanso mogwirizana ndi Yunivesite ya Strathclyde, tidayambitsa ntchito yokumba mijigo ndipo malo 6 mwa 7 omwe anabowoleredwa anali amchere choncho tidagwiritsa ntchito malo omwe anali ndi madzi aukhondo ndi kugawa madzi otetezeka kumadera ambiri," anatero a Mtegha.

Iwo anati ntchitoyi inagwiritsa ntchito ndalama zokwana 127,000 ndalama zaku Amerika ndipo pano bungweli liri ndi makina opopa madzi oyendera mphamvu ya dzuwa okwana 19 omwe ali mmadera a m'bomali.

"Ntchito yamadzi ya Tsamba ndiyonyaditsa kwa ife popeza ndi imodzi mwa ntchito zamadzi zikulu zikulu mdziko muno, yomwe anthu akupindula nayo" anatero a Mtegha.

Ntchitoyi yakhudza mbali zambiri zachitukuko kuphatikizapo zamaphunziro, zaumoyo ndi zachikhalidwe ndi chuma cha anthu.

Wachiwiri kwa wapampando wantchito ya madzi ya Tsamba, a Patrick Chalonda anati akhala m'mudzi mwa Tsamba kwa zaka 60 akupirira mavuto a madzi omwe amakhudzanso midzi ya Meja ndi Paiva.

"Chitukuko cha madzi chasintha miyoyo yathu kuno. Maganizo athu tsopano amapita kutsogolo lana athu ndi mavuto ena osatinso madzi ayi," anatero a Chalonda.

Iwo anatinso pofuna kupititsa patsogolo chitukukochi anthu anagwirizana kuti azipereka ndalama yochepa yokwana 10 kwacha akamatunga madzi.

"Ndalamazo ndi zothandizira chitukukochi moti pano tasungako ndalama yopitirira K1miliyoni kuthumba lathu," anatero iwo.

Mkulu owona zamadzi m'boma la Chikwawa, a Rester Msuza, anati chitukuko chamadzi cha Tsamba chathandiza anthu oposa 4000 ku mavuto a madzi ndipo anthu ambiri ku Chikwawa tsopano ali ndi madzi otetezeka chifukwa cha kuyesetsa kwa boma kudzera ku thandizo la Water for People, Water Mission, CICOD, Islamic Relief, Unicef ndi ena othandizana nawo.

Iwo anawonjezeranso kuti m'zaka 60 zapitazi, boma la Chikwawa lasintha pamene m'mbuyomu chigawochi chinkakumana ndi vuto la kusowa kwa madzi, limene limavutitsa amayi ndi ana.

"Vutoli linkafunika kuchitapo kanthu ndipo boma linagwirizana ndi mabungwe achitukuko kuti akhazikitse chitukuko cha madzichi.

Ntchitoyi imaperekanso mijigo mmadera onse a m'bomali pothana ndi kusowa kwa madzi mmaderawa.

Msuza anatinso: "Pofika m'chaka cha 2023, tinali titakhazikitsa mapampu opopa madzi okwana 58, pamene mijigo inali 3,634 ndipo cholinga chathu tsopano ndikuwonesetsa kuti madzi a m'mipopi afikere m'malo onse ochitira malonda komanso kuti munthu aliyense wa ku Chikwawa apeze madzi a ukhondo ndi otetezeka."

Mlembi wamkulu mu unduna wa za madzi ndi ukhondo, a Elias Chimulembe, anagwirizana ndi a Msuza ponena kuti Boma ndilodzipereka kubweretsa madzi a ukhondo kwa Amalawi onse pomanga masikimu a madzi ochuluka kumadera akumidzi.

A Chimulembe anati chitukuko cha zomangamanga zoterezi chikhoza kuthetsa mavuto a madzi m'madera akumidzi, mogwirizana ndi cholinga cha boma powonesetsa kuti pofika chaka cha 2030 anthu onse adzapeze madzi a ukhondo, monga momwe zinalongosoledwera mu chikalata cha cholinga cha chitukuko chokhazikika cha bungwe la United Nations cha nambala 6.



*Mayi Selena kunyadira madzi abwino pa mpope*



*Chitukuko chamadzi aukhondo ku Tsamba, m'boma la Chikwawa*

**DR. HASTINGS KAMUZU BANDA**

Uyu ndi Mtsogoleri oyamba wa dziko la Malawi amene anachotsa dzikoli mu ulamuliro wa atsamunda wa boma la Britain ndikuyika Malawi pa ufulu odzilamulira tokha mchaka cha 1964. Mwa zina a Banda anakhazikitsa maphunziro apa mwamba pokweza mwayi wopita ku sukulu za pulaimale ndi sekondale.

Iye anapititsa patsogolo chitukuko cha chuma kudzera muntchito szomangamanga ndi ntchito zaulimi.

1964





1994

**DR. BAKILI MULUZI**

Bakili Muluzi ndi Mtsogoleri wachiwiri amene anatenga boma kuchoka ku ulamuliro wa MCP ndikutsogolera kuyambitsa ulamuliro wa demokalasi wa zipani zambiri popereka ufulu pa ndale. Iwo adakhazikitsanso kusintha kwachuma, kubweretsa sndalama zakunja ndikulimbikitsa mwayi wopeza maphunziro poyambitsa maphunziro a ulele aku Pulayimale.

**PROF. BINGU WA MUTHARIKA**

Bingu wa Mutharika ndi mtsogoleri wachitatu wa dziko la Malawi amene analamulira Malawi kuchoka mchaka cha 2004 mpaka 2012. Mwazina Mutharika anathandiza Kusintha kwachuma, ndi kupititsa patsogolo ntchito zosiyanasiyana za chitukuko. Iwo anathandizira kukweza chitukuko cha zomangamanga, kuphatikizapo misewu ndi ulimi wanthirira. Mutharika anathandiziranso kuwonjezera ndikutukula maphunziro a pulayimale ndi sekondale.

2004





2012

**DR. JOY**

Joyce Ba
oyamba w
dziko la M
dzikoli ku
mpaka 20
umadziwi
uchembe
kulimbikit
makamak

A Banda
atolankha
mabungw
wamalon
ufulu wac
pakati pa
mdzikoli.

# ATSOGOLERI AMENE ALAMULIRA DZIKO LINO MU ZAKA 60 ZA UFULU

**PROF. ARTHUR PETER MUTHARIKA**

Peter Mutharika analamulira Malawi kuchoka mchaka cha 2014 kufika mchaka cha 2020. Munthawi yake ya utsogoleri Mutharika adachita zinthu zosiyanasiyana zabwino. Iye adayika ndalama pa zachitukuko, kuphatikiza ntchito zomanga misewu ndi mphamvu zamagetsi. Mutharika adayikanso patsogolo maphunziro, kukulitsa mwayi opita ku pulayimale ndi sekondale komanso kuyambitsa njira zotukula maphunziro a aphunzitsi ndi zotsatira za ophunzira. Kuphatikiza apo, adalimbikitsa chuma cha dziko. Adayesetsanso kulimbikitsa ntchito za umoyo, kuphatikizapo kukulitsa ndondomeko za chithandizo cha HIV/AIDS komanso kumanga zipatala zatsopano.



**2014**



**2020**



**LERO**

**CE BANDA**

nda anali mtsogoleri wachizimayi kulamulira Malawi, iye analamulira choka mchaka cha 2012 014. Utsogoleri wawo ika bwino ndikulimbikitsa le wabwino komanso tsa maphunziro ka a atsikana.

analimbikitsanso ufulu wa ani komanso kuthandizira we azamalonda ndi mwayi dawo, analimbikitsanso chibadwidwe ndi kufanana amuna ndi akazi

**DR. LAZARUS MCCATHY CHAKWERA**

Kuyambira pomwe anatenga udindo wa mtsogoleri wa dziko mu 2020, Purezidenti Lazarus Chakwera wachita zinthu zingapo zabwino ku chitukuko cha dzikoli. Iye waika patsogolo ulamulilo wabwino, kuyambitsa kampeni yolimbana ndi katangale ndi kukhazikitsanso bwalo la milandu lothana ndi katangale.

A Chakwera adatsindikanso za chitukuko cha chuma, kuyambitsa ndondomeko zokopa anthu akunja komanso kulimbikitsa bizinesi. Iye Waika ndalama zankhani nkhani pamaphunziro, ndipo akuwonjezera ndalama zamasukulu ndi kuyambitsa njira zowonjezera maphunziro a aphunzitsi ndi zotsatira za ophunzira.

Kuonjezera apo, a Chakwera ayesetsa kupititsa patsogolo ntchito za umoyo, kuphatikizapo kukulitsa mwayi wopeza katemera wa COVID-19 komanso kukonza zomangamanga m'zipatala za boma.

Iye walimbikitsanso kufanana pakati pa amuna ndi akazi ndi kupatsa mphamvu amayi, akuyambitsa njira zothandizira amalonda achikazi ndi kuthana ndi nkhanza zomwe amayi amakumana nazo. Utsogoleri wa Chakwera wadziwika ndi kudzipereka pakuchita zinthu mwapoyera ndikulimbikitsa chitukuko cha m'madera onse ndi cholinga chofuna kusintha dziko la Malawi kuti likhale dziko lotukuka komanso lachilungamo.

# Madzi abwino ndiofunika - Kakhobwe

WOLEMBA:
MARTIN CHIWANDA

ZA MADZI



Zipangizo za Ntchito ya chitukuko chamadzi ku Dowa

KUPEREKA madzi abwino kwa onse ndi chimodzi kwa zokhumba za Boma pofika chaka cha 2063. Kusowa kwamadzi a ukhondo lidakali vuto mmadera ena adziko lino.

Boma lati ntchito idakalipo yowonesetsa kuti anthu onse mdziko lino akulandira madzi abwino otetezeka kumatenda popititsa patsogolo umoyo wa anthu.

Wachiwiri kwa Nduna ya Zamadzi ndi Ukhondo, Liana Kakhobwe Chapota ananena izi posachedwapa atayendera madzi a mmipope yomwe inamangidwa ndi bungwe la Self Help Africa ku Mtungwi mdera la Mfumu yayikulu Chiwere ku Dowa.

Ndunayi inati mabungwe ogwira nawo ntchito yopereka madzi abwino kwa anthu ndi ofunikira chifukwa amathandizira ndi kukwaniritsa zomwe boma likuchita potukula ntchito za chitukuko chamadzi.

Dera lomwe ndunayi idayendera linali lomwe anthu 288 anadwala matenda a Kolera ndipo anthu asanu ndi awiri anataya miyoyo matendawa atavuta mchaka cha 2022 kufika cha 2023.

"Derali lidakhudzidwa kwambiri ndi matenda a Kolera mchaka cha 2023 chifukwa anthu ambiri analibe madzi akumwa a ukhondo. Ndife okondwa kuti lero kuli mipope ndipo ndizosangalatsa kuti chaka chino sikunabuke matenda a Kolera.

"Ndimabungwe ochepa omwe amafikira anthu ndi zinthu zogwirika monga taonera pano, tikuthokoza kwambiri chifukwa chachitukukochi," anatero Kakhobwe.

Wachiwiri kwa Ndunayu analimbikitsa anthu kuti ayang'anire bwino zipangizo zamipopezo kuti akhale akugwiritsa ntchito kwa nthawi yayitali.

Mkulu wa bungwe la Self Help Africa, Snowden Tomoka anati ntchito yoyika mipopeyi yomwe ndiyandalama zokwana 60 miliyoni kwacha ithandiza mabanja okwana 400 omwe ndi anthu pafupifupi 2,000.

A Tomoka adati bungweli linaganiza zobweretsa ntchito yamadziyi chifukwa derali ndi limodzi mwamadera omwe anakhudzidwa ndi kolera mmbuyomu.

M'modzi mwa anthu omwe apindula ndi ntchito yamadzi abwinowa, Chikondi Chiwiya wa mmudzi mwa Mndola anati kale anthu amakatunga madzi okumwa mumtsinje zomwe zimabweretsa chiwopsezo pamiyoyo yawo.

WOLEMBA
RENNIE TEMBO

# Aphunzitsi aphunzira kuthana ndi nkhanza

ZA MAPHUNZIRO



Apolisi kuphunzitsa amphunzitsi zoteteza ophunzira ku Nkhanza

APOLISI ku Lilongwe akhazikitsa ntchito yotetedza ana powadziwitsa za maufulu awo yomwe ikutchedwa 'Sukulu zotetezeka' yomwe ichepetse nkhanza kwa ophunzira.

Polankhula pamaphunziro omwe anakonzedwa ndi apolisi a ku Lilongwe, mkulu oyang'anira zachitetedzo chammadera, a Frank Kayira anati cholinga cha ntchitoyi ndikupanga sukulu kukhala malo otetezeka kwa ophunzira komanso kuthandiza aphunzitsi ndiluso la momwe angathanirane ndi nkhanza mmasukulu.

A Kayira anati ntchitoyi inayamba ngati njira imodzi yothana ndi nkhanza zambiri zomwe zakhala zikubwera ku polisi kuyambira mwezi wa Januwale mpaka Meyi chaka chino.

"Takhala tikuphunzitsa msukulu ngati mbali imodzi yantchito yathu mmaderamu. .Aphunzitsi amakhala oyamba kulandira nkhani zankhanza kuchokera kwa ophunzira mmakalasi," anatero Kayira

Pofuna kulimbikitsa ophunzira kuti azinena momasuka zankhanza zomwe amakumana nazo, mabokosi oponyamo timapepala tolembapo madandaulo awo ayambitsidwa msukulu.

"Tayambitsa mabokosi oponyamo madandaulo m'masukulu kuti ophunzira azitha kuyika madandaulo awo. Iyi ndi njira yabwino yowonetsetsa kuti palibe amene akuwaletsa kulankhula momasuka pazomwe amakumana nazo," anatero Kayira.

Iwo analimbikitsa aphunzitsi kuti aziwonetsetsa ndi kutsatira makhalidwe a ophunzira kuti azitha kudziwa mwachangu zomwe zikuwachitikira ndi kudziwa ngati akukumana ndi nkhanza mmoyo wawo..

Mlangizi wamkulu wa zamaphunziro a Caroline Chiwayula anayamikira ntchitoyi yomwe anati ithandiza kwambiri kuchepetsa nkhanza mmasukulu .

"Pali nkhanza zambiri zomwe ophunzira amakumana nazo kuchokera kwa aphunzitsi ndi ophunzira anzawo ndipo zina mwankhanzazi zimakhala zovuta kuzizindikira ndikuthana nazo kwake. Koma ntchitoyi ithandiza kupereka chidziwitso chomwe tinkasowa pakusamalira ophunzira omwe akukumana ndi nkhanza zosiyanasiyana," anatero Chiwayula

Iwo anadandaulanso kuti pali nkhanza zina zomwe aphunzitsi amalandira kuchokera kwa ophunzira ena.

"Mudziwe kuti timakumana ndi nkhanza zosiyanasiyana kuchokera kwa ophunzira makamaka omwe akugwiritsa ntchito mankhwala osokoneza bongo. Timakumananso ndi nkhanza kuchokera kwa makolo ena omwe amagwiritsa ntchito udindo wawo wakuntchito, zomwe zimakhudza ntchito yathu," iwo anatero.

Ntchitoyi igwiridwa m'masukulu khumi ndi imodzi m'boma la Lilongwe.

# GESD ilimbikitsa atsikana pomanga zipinda zogona mmasukulu

WOLEMBA:
LEAH MALIMBASA


Thokozile Munthali - Mkulu woona za dongosolo ndi chitukuko pa khonsolo la boma la Chikwawa

ZA MAPHUNZIRO


Freeds Malata, mphunzitsi wankulu pa Ching'amba sukulu

Wojambula: Nkhokwe yathu

NTCHITO yothandiza kupereka zitukuko mmaboma ya GESD, ikuthandiza kutukula magawo ambiri achitukuko mmaboma monga ku Chikwawa.

Kumangidwa kwa nyumba yogonamo atsikana pa sukulu ya sekondale ya Ching'amba ndi ndalama zokwana K86.2 miliyoni zochokera ku Banki yaikulu padziko lonse ya World banki, yasintha zinthu pasukuluyi.

Nyumbayi, yomwe yamangidwa mdera la Mfumu yaikulu Chapananga, simalo ongogonerako chabe koma ndi njira ya tsogolo lowala la Mangalita England, mtsikana wa zaka 17 komanso ophunzira ena achichepere okwana 122.

England anati: "Kwa zaka ziwiri, ndayenda maulendo aatali ndi otopetsa, ulendo uliwonse ndimayenda pafupifupi ola limodzi kuchokera kumudzi kwathu kupita ku sukulu.

Iye adafotokoza kuti amanyamuka m'mawa ndi cholinga chakuti akafike ku sukulu nthawi yabwino, koma anati nthawi zambiri amachedwa chifukwa cha sitima imene imadutsa pa njira yopita ku sukulu kwawo, zomwe zimamupangitsa kuti achedwe.

Mphunzitsi wamkulu wa pa sukulu ya sekondale ya Ching'ambika, a Freeds Malata, anati sukuluyi idatsegulidwa m'chaka cha 1992 ndipo kwa zaka 32, ophunzira ochokera m'midzi yakutali amapirira mitunda yotereyi kuti akapeze maphunziro.

Koma kumangidwa kwa nyumba yogonamo atsikanayi, kupititsa patsogolo chiwerengero cha ophunzira opezeka pa sukuluyi.

"Poyamba tinakumana ndi zovuta komanso kutsutsana ndi anthu ena a m'mudziwu, makamaka pankhani ya umwini wa malowa. Ndinakhazikika pachikhulupiriro chakuti mtsikana aliyense amayenera kupeza maphunziro apamwamba," anatero a Malata.

Kupirira kwawo polimbana ndi zopingazi kunabweretsa chilolezo chimene chinkafunikira ndi kulimbikitsa mgwirizano ndi umodzi pakati pa anthu a mderali.

Iwo anati: "Ntchito yomanga nyumbayi yatha ndipo tikungodikira kuti ilumikizidwe ndi madzi komanso magetsi kuti atsikanawa alowemo.

Izi zikachitika, atsikanawa azasiya kuyenda mitunda itali itali, komanso kuchedwa ndi kayendedwe ka sitima zizathera pompo. M'malo mwake, azichita maphunziro awo mosada nkhawa, podziwa kuti malo otetedzeka alipo pasukulu pompano,"

Mkulu wa bungwe lowona za maphunziro atsikana, a Limbikani Kamlongera, anagwirizana ndi a Malata ponena kuti kukhala m'nyumba zogonera pa sukulu ku Malawi kuno ndi kofunikira pazifukwa zingapo.

Iwo anati: "Kumapereka malo abwino ophunzirirapo komanso otetezeka ku zovuta zosiyanasiyana za chikhalidwe ndi zina zimene zingawalepheretse atsikana maphunziro awo.

Iwo anatinso kugonera pa sukulu kumalimbikitsa ubale ndikuthandizana pakati pa atsikana, zimenenso zimalimbikitsa mgwirizano.

"Mwachidule, malo ogona pa sukulu amathandizira kwambiri powonetsetsa kuti atsikana akumidzi m'Malawi muno akupeza mwayi okachita maphunziro awo m'malo otetedzeka komanso osamalidwa bwino, zomwe zingawakonzere tsogolo la bwino," anatero a Kamlongera.

Padakali pano, Mkulu owona za dongosolo ndi chitukuko pa khonsolo la boma la Chikwawa, a Thokozile Munthali, anati ophunzirawa ayamba kugwiritsa ntchito nyumbayi chaka cha maphunziro chikubwerachi kuti amalizitse kulumikiza madzi, magetsi, komanso kuwonjezera mayenje a zimbudzi.

"Timadziwa kufunika kwa malo ogona pa sukulu; ndichifukwa tikumanga nyumba zogona zambiri m'boma lino mu dongosolo lathu la chitukuko cha boma," anatero a Munthali.

Zotsatira za kafukufuku wa World Banki zikuwonetsa kuti sinkhanza zokha zomwe zimalepheretsa atsikana sukulu komanso kuyenda mitunda yaitali zimene zimawayika paziwopsezo zowalepheretsa maphunziro.

Chiwerengero chaposachedwapa chikusonyezanso kuti atsikana pafupifupi 60 miliyoni amagwiriridwa popita kusukulu chaka chirichonse.


Mangalita England, ophunzira pasekondale ya Ching'amba

ZA MISEWU



Wojambula: Vincent Khonje

*Ena mwa malo oyipa mu nsewu wa Mangochi - Makanjira*

# Anthu ku Makanjira ali ndi chiyembekezo cha nsewu watsopano

WOLEMBA
BISHOP WITMOS

MWEZI wa Novembala chaka 2023, unali mwezi wosangalatsa ku dziko la Malawi. Mmweziwu Mtsogoleri wa dziko lino, Lazarus Chakwera, anakwera ndege kupita ku Riyadh, mdziko la Saudi Arabia, kukasayina pangano la ndalama zokwana 20 Miliyoni zaku Amerika kuti zigwire ntchito yomanga msewu ochokera ku Mangochi Boma kupita ku Makanjira.

Mtsogoleri wadziko lino anabwerera kuno kumudzi akumwetulira, powona kuti mavuto amene anthu aku Makanjira amakumana nawo chifukwa cha nsewu oyipa azakhala mbiri yakale.

Mfumu yayikulu Makanjira, yomwenso inali komweko ku Riyadh, kukachitira umboni pa mwambo osayinira ntchitoyi, nawonso anabwerera kumudzi akumwetulira.

''Ndinalipo nthawi yomwe a Chakwera amalandila chitsimikizo chakuti dziko la Saudi Arabia lipereka ndalama zomangira nsewu wa Makanjira. "Uwu ndi mwayi waukulu kwa anthu anga, msewu wa phula uja ukubwera ku Makanjira,'' anatero a Makanjira.

Pofika mwezi wa Epulo, 2024, anthu a ku Mangochi anayamba kuwona ntchito yomanga msewu ikuyambika.

Msewu opita ku Makanjira unali ovuta ndipo unalinso ndi mayenje ambiri, pachifukwa ichi, anthu amatuwa kwambiri asanafike kuderali.

Pa ulendo wathu okawona derali tinali ndi mavuto kuti tijambule zithunzi pa ntchito yathu. Anthu kuderali amaletsa kujambula zithunzi chifukwa amati atopa ndi anthu ongojambula mavuto ansewu wawo koma popanda chochitika chili chonse.

Wina analanda makina athu ojambulira zithunzi ndi kutikakamiza kufufuta zithunzi zotere, ponena kuti chinali chipongwe kujambula zithunzi zoterezi pamalopo.

''Takuwonani anyamata inu mukujambula zithunzi zingapo mumseuwu kwa nthawi yayitali, ndipo ngati anthu ammudzi muno tatopa ndi mchitidwewu. Fufuta chithunzi chirichonse chomwe munatijambula," anatero dalaivala wina wokwiya.

Izi zinafowoketsa chidwi changa chofuna kusangalala ndi ulendowu popeza ndinali ndi mantha. Koma mantha anachoka pamene tinali nawo pamkumano okambirana za nseuwu, pomwe mafumu anatitsimikizira kuti tigwire ntchito momasuka ndikulemba zanseuwu.

''Musachite mantha inu gwirani ntchito yanu, mutitengere mavuto omwe ali kuno kwathu,'' anatero Mfumu yaikulu Katuli pazokambiranazo.

Anatiwuza momwe msewu wa Mangochi kupita ku Makanjira walepheretsera chitukuko cha chuma kuderako komanso kudziko la Malawi kwazaka zambiri.

"Dera lathu lino ndi lolemera. Ndilodalitsidwa ndi dothi la chonde ndichifukwa chake mbewu zambiri ndi nsomba zomwe zimapezeka mtauni ya Mangochi, mpaka mmizinda ya Blantyre ndi Lilongwe zimachokera kuno,''

"Kwa zaka zambiri tsopano, mseu wathu wakhala uli oyipa kwambiri," anatero a Katuli.

Mawuwa anatipangitsa kuganizira zamomwe anthu okhala kumpoto kwa Mangochiwa amavutikira poyenda mseu wa makilomita 120, omwe umatenga mawola anayi kuti apaulendo akafike pa boma la Mangochi.

Tinayamba kuwerengera milatho ikuluikulu yomwe inapita ndi namondwe wa Freddy yemwe anachitika posachedwapa ndipo inali yoposa 10.

poyendera mseuwu, titatsala pang'ono kufika pa Makanjira, lomwe ndi dera la anthu oposa 120 000, tinafika pa mlatho waukulu ochititsa mantha omwe unamira mumtsinje.

Apa, anyamata ena anapezerapo mwayi pa vutoli ndipo anachita zotheka kuti anthu adutse mtsinjewo. Tinalipira K2000 kuti tipeze mwayi odutsa.

Izi zinatikumbutsa mawu a Mfumu yaikulu Makanjira pamene a Chakwera anayendera derali nthawi imene amakakhazikitsa ntchito yomanga nyumba yoperekerako chisamaliro cha azimayi oyembekezera pa Chipatala cha Makanjira imene idamangidwa ndi ndalama zokwana K2.5 biliyoni.

Mfumu Makanjira inanena zankhani ya za umoyo m'dera lawo, ponena kuti amayi ndi ana ambiri ataya miyoyo yawo mzaka khumi zapitazi pofuna kupeza chithandizo cha amayi oyembekezera pachipatala chachikulu cha Mangochi.

"Amayi ambiri amachirira mumseu ndipo ena ambiri amwalira panjira yopita ku chipatala cha Mangochi chifukwa cha kuwonongeka kwa miseu."

Mfumuyi inati kupatula nkhani za uchembnbere, mseu watsopano omwe anthu akuyembekezera ku Makanjira uzathandiza kutukula derali ndimadera onse ozungulira pankhani ya ulimi, malonda komanso za umoyo wa aliyense popeza kuti mayendedwe azakhala osavuta kuderali.



*Ndinali nawo posainira za nsewu wathu - Mfumu yaikulu Makanjira*

# Stich Fray wabweranso ndi chimbale

WOLEMBA
PEMPHO NKHOMA

KATSWIRI ojambula ndi kuyimba nyimbo mu mzinda wa Blantyre, Steven Chibwazi, yemwe amadziwika kwambiri ndi dzina lakuti Stich Fray, watulutsa chimbale chotchedwa Mtendele.

Polankhula ndi nyuzi pepala ya Boma Lathu, Stich Fray anafotokoza chifukwa chimene anakhalira chete pankhani za mayimbidwe ponena kuti amafuna kubwera ndi "nyimbo zotentha".

"Ndinatenga nthawi ndisanatulutse nyimbo chifukwa ndinafuna ndipeze mfundo zokhwima. Ndinali otanganidwa kupanga zimbale za oyimba ena zomwe ndimajambula ku malo anga ojambulira nyimbo," anatero.

Stich Fray wapanga chimbale cha nyimbo 10 zomwe ndi; Hello, Ah Abale, Ndimafuna Mtendele, Nkhawa bii, Shu Shu Shu (kwayaka moto), Ine si Nep Man, Gentleman, Mzanga, Wagwa komanso Still Me.

Iye anati chimbalechi chikulimbana ndi zinthu zambiri koma chakhazikika pamutu wa mtendere ndi chikondi monga momwe mutu wake ukunenera.

Stich Fray anafotokozanso kuti anasakaniza mitundu yosiyanasiyana ya mayimbidwe mu chimbale chake chatsopanochi kuti athe kufikila anthu osiyanasiyananso.

"Ndangosakaniza mitundu ya mayimbidwe a nyimbo kuti aliyense athe kupeza mtundu wanyimbo zomwe amakonda kumvetsera," anatero oyimbayu.

Iye ananenanso kuti anayimba ndi akatswiri ena odziwika bwino monga Nep Man, malemu Evison Matafale mu (Nkhawa bii cover), DNA, Leumas, Queen Fire, Annie Matumbi ndi Smacks.

Mmodzi mwa omutsatira oyimbayu, Alfred Kalikokha, anakondwera ndi chimbale cha Stich Fray cha tsopanochi ponena kuti Stich Fray ndi oyimba yemwe amamukonda kwambiri ndipo amachiyembekezera mwachidwi chimbalechi.

"Stich Fray ndi oyimba yemwe ndimamkonda kwambiri, ndimakonda nyimbo zake ndipo ndimachiyembekezera chimbalechi," anatero.

Chimbalechi chipezeka kwaulere m'mawebusayiti onse a nyimbo monga Malawi Music.com, Mikozi Network ndi Makosana mwa ena.


Stich Fray

Wojambula: Nkhokwe yathu




# Jetu, gogo oyimba wavuta pa Malawi



Jetu omwe dzina lawo lenileni ndi Christina Kholiyo

WOLEMBA
PEMPHO NKHOMA

PAMENE anthu okalamba ali pachiopsezo ndi zauchifwamba zimene zakhala zikuchulukira mdziko muno, mayi wina wa zaka 71, Christina Kholiyo, akuchita zinthu zodabwitsa zimene zatekesa dziko la Malawi komanso maiko ena ozungulira kumbali ya msangulutso.

Mayiyu, yemwe akudziwika bwino ndi dzina lakuti Jetu, amakhala ku Bangwe, mumzinda wa Blantyre, ndipo posachedwapa watulutsa nyimbo yatsopano yachamba cha makono cha Amapiano imene akuitcha kuti 'Chakwaza,' mau amene mayiyu wagwiritsa ntchito munyimboyi potanthauza kuti ndalama.

Kanema wanyimboyi adapangidwa ndi Emu Dee, amene ali mdzukulu wa Jetu, ndipo pakanthawi kochepa kokha wafikira zikwi za anthu opitirira 819,000 pa tsamba la mchezo la You Tube lokha, ndikukopa anthu amdziko muno komanso amayiko ena pa masamba amchezo osiyanasiyana.

Ena mwa omutsatira oyimbayu ochokera kumaiko osiyanasiyana anakhamukira kumasamba amchezo apa intaneti kumene amawonera ndi kuwonetsera chikondi chawo pa kanema wanyimboyi mundemanga zawo.

Mmodzi mwa otsatirawa adati: "Jetu ndi katswiridi ndipo kanemayi ndamuwonera kangapo chifukwa ndi opatsa chidwi. "Tili pambuyo panu mayi Jetu, landilani moni kuchokera kuno ku Nigeria," adateronso otsatira wina pothirira ndemanga.

Pamene ambiri akuyamikira za luso la gogoyu, ena akhala akudandaula za msinkhu wa Jetu ndikupereka mafunso pa zolinga za zidzukulu zake zimene zikumuthandiza Jetu pa luso lake la mayimbidwe.

Ena akuti Jetu ndi okalamba kwambiri ndipo asakhale nawo mgawo la akatswiri amsangulutso a mdziko muno pamenenso maganizo a ena akuti gogoyu akugwiritsidwa ntchito ndi adzukulu ake kuti apezerepo ndalama.

Poyankha, Jetu adakanitsitsa, ndipo adatsimikizira anthu kuti iye wakhala moyo osangalala kuyambira kale asadatchuke.

Iye adati: "Kutchukaku kwangopereka mwayi owonetsera ku mtundu wa anthu moyo wa chimwemwe umene ndimakhala nthawi zonse."

Kumbali yake, Emu Dee movomerezana ndi agogo ake anapempha onse owatsatira kuti avomereze chisankho chimene Jetu anapanga ndikuchilemekeza.

"Zimene ine ndi agogo anga timapanga ndizolimbikitsa chisangalalo ndi mgwirizano," anatero pofotokoza.

NTHANO

# Asochela mu mzinda wa Lilongwe

WOLEMBA
LEONARD MASAULI



MKHALIPI anali wachichepere pomwe makolo ake a Kamuganje ankasamuka kupita ku theba mdziko la Zimbabwe mchaka cha 1964. Bambo Kamuganje anali atanunkhiza kuti ku dziko la Zimbabwe kunali mkaka ndi uchi. Chifukwa cha mavuto ena omwe analipo iwo adaganiza kuti apite ku Theba akapumiseko zolema zakumunda ndikukayendako pamwamba pa Bread.

Kamuganje adali mlimi yemwe dera lakwawo lonse amatchuka ndi kulima minkhaka komanso mavwembe omwe amagulitsa kutauni ndipo amakwanitsa nkumapeza zosowa za pabanja pawo. Koma patapita nthawi iwo adaganiza zokayesa mwayi ku dziko la Zimbabwe komwe amakagwira ku migodi. Mwansangansanga anakwera mathilaki onyamula chimanga.

Pakafika ku Zimbabwe, Kamuganje ndi banja lake sanapeze zomwe amayembekezera. Ntchito ya ku migodi inali yovuta kwambiri, ndipo ndalama zimene amalandira sizinali zokwanira. Iwo anayamba kuzindikira kuti moyo unali wovuta kwambiri. Koma Kamuganje sanataye mtima; anaganiza zopita ku mzinda wa Harare kukafunafuna mwayi wina.

Mkhalipi, mwana wawo wamkulu, anayamba sukulu ku Harare ndipo anali mwana wanzeru kwambiri. Sukulu imene anaphunzira inamupatsa mwayi wokacheza kumayiko akunja kudzera mu mpikisano wa sayansi. Izi zinapangitsa banja la Kamuganje kuyamba kuwona kuwala kutali. Mkhalipi atapambana mpikisano, anapita ku South Africa komwe adapitiliza maphunziro ake aukachenjede.

Pamene Kamuganje anali kugwira ntchito molimbika ku Harare, mkazi wake adachita bizinesi yaying'ono yogulitsa masamba pamsika. Izi zinawathandiza kuti apeze ndalama zowonjezera ndiponso kuonjezera zomwe anakwanitsa kupeza.

Patapita zaka zingapo, Mkhalipi anamaliza maphunziro ake ndikubwerera ku Zimbabwe ngati dokotala. Izi zinabweretsa chimwemwe chachikulu kubanja la Kamuganje, chifukwa tsopano anali ndi munthu yemwe angawathandize kukwaniritsa maloto awo.

Mkhalipi atabwerera ku Zimbabwe, sanaiwale kwawo ku Malawi. Anayamba pulogalamu yaumoyo yomwe inkathandiza anthu a m'dera lakwawo ku Lilongwe. Anapereka chithandizo chamankhwala kwaulere ndikumanga zipatala.

Banja la Kamuganje linasamukira ku Malawi kachiwiri atawona kuti moyo wawo watha kukhala wabwino. Kamuganje adakhalabe mlimi, koma tsopano anali ndi thandizo la mwana wake Mkhalipi amene anali dokotala wotchuka.

Komabe, tsiku lina atabwerera ku Lilongwe kuchokera ku ntchito zawo zakumunda, banja la Kamuganje lidapeza kuti mzinda wa Lilongwe unasintha kwambiri. Panali misewu yatsopano komanso milatho yokongola, zomwe zinawapangitsa kuti asowe njira yobwerera kunyumba yawo ku Area 25. Atazungulira mzinda kwa masiku angapo, Kamuganje ndi banja lake anayamba kuda nkhawa.

Mkhalipi, yemwe anali atakula ndi kuphunzira bwino, adaganiza zothandiza banja lake kuti asapezeke ali osowa choncho. Iye anapita ku shopu ina n'kukafunsa anthu njira yobwerera ku Area 25. Anthu a ku shopu anali okoma mtima ndipo anawatsogolera bwino.

Pomaliza, Kamuganje ndi banja lake anafika kunyumba kwawo ku Area 25 atakumana ndi zokumana nazo zosaiwalika mumzinda wosinthika wa Lilongwe.


Apa m'pomwe Kamuganje adazindikira kuti ngakhale moyo umasinthasintha, kupitapita kumudzi ndi chinthu chamtengo wapatali chifukwa umadziwa mene dziko likuyendera.

Iye anadzimvera chisoni kuti sanathe kuzindikira komwe akanalowera chifukwa kwa dzaka zokwana 60 tsopano Mzinda wa Lilongwe unali ngati komwe ku Zimbabwe misewu yabwino yoyendamo magalimoto ambiri komanso milatho yomwe nkale lonse kunalibe.

Iwo anagwira mchiuno naomba m'manja kuti phu phu phu uku akupukusa mutu kuti dzaka 60 zomwe anakhala kutheba analuza zambiri kuona dziko la Malawi likumwemwetera ndichitukuko.

MPONDO

Peter Nyakhuwa



# Katswiri wamasewero osambira, Chang'anamuno wakonzeka

WOLEMBA
TWIMEPOKI MANGANI

OSAMBIRA odziwika bwino mdziko muno, Tayamika Chang'anamuno anali ndi chisangalalo chachikulu atapeza mwayi wokayimirira dziko la Malawi pa mpikisano wa Olimpiki wa chaka cha 2024 ku mzinda wa Paris mdziko la France.

Polankhula ndi Boma Lathu, iye anati mwayiwu ndi ulemu waukulu komanso zotsatira za kudzipereka komanso kulimbikira kwake.

"Ndili okondwa kukachita nawo mpikisano wa olimpiki ku Paris, ichi chakhala cholinga changa kuyambira ndili wachichepere ndipo kwazaka zambiri, ndadzipereka komanso wosasunthika ndipo pamapeto pake zapindula," anatero Chang'anamuno.

Pamene masewerowa akuyandikira, iye anayika maganizo onse pakukonzekera ndi kulimbitsa thupi lake mothandizidwa ndi aphunzitsi ake.

"Ndili ndi aphunzitsi ozipereka kotero ndili ndi chikhulupiliro kuti ndikhala okonzeka bwino kukachita nawo mpikisano wapamwambawu."

"M'kati mwamasewerowa, ndikuyembekeza kukakwanitsa nthawi yanga bwino komanso kukapanga mbiri yadziko langa posambira mmalipande 50.

Nthawi yanga yokonzekera ndayika yambiri kuti ndizikonzekeretse bwino ndikuphunzira kupirira komanso kulimbitsa thupi ndikupanga zinthu mwachangu pamene tikuyandikira mpikisanowu, " iye anatero.

Mphunzitsi wa akatswiri osambira mdziko muno, a Yona Walesi anatsimikiza kuti Chang'anamuno ndi Filipe Gomez ndi omwe akayimire dziko la Malawi pa mpikisano wa Olimpikiwu pamene anati akatswiriwa ndiodzidalira komanso olimbikira pa luso lawo.

"Osambira athu awiriwa, akapikisana nawo pa malipande 50 owonetsera luso lawo, ndipo pano awonetsa kale luso lapadera pamene akukonzekera mozipereka. "

"Ndikuyembekeza kuti akachita bwino pochepetsa nthawi yawo yosambirira pamtunda operekedwawo. Iwo akonzekera mwamphamvu kuti apeze mwayi umenewu, ndipo ndikukhulupirira akayimirira bwino dziko la Malawi ," anatero.

A Walesi analimbikitsa onse omwe atakachite nawo mpikisanowu kuti akachite zomwe angathe kuti azakondweretse dziko la Malawi ndi chipambano.

Ngakhale patakhala kusintha kwina pamasewerowa osambira a Olimpiki, Chang'anamuno ndi Gomez akuyembekezeka kusewera nawo mpikisano wa malipande 50 ndikuwonetsera luso lawo.

Chang'anamuno, yemwe ndi wazaka 22, ali ku Budapest, mdziko la Hungary pa maphunziro a zaka zinayi, pamene Filipe Gomez, wazaka 25, akukonzekera ndi timu yake ku dziko la Portugal pansi pa maphunziro okonzekera masewero a Olimpikiwa.

Masewera a Olimpiki ayamba pa 26 Julaye, mpaka pa 1 Ogasiti, 2024 ndipo mpikisano osambira ukayamba pa 27 Julaye ku bwalo la masewera la Paris.



*Tayamika Chang'anamuno katswiri wamasewero osambirira*

# Masewero ampira wamiyendo wa atsikana ukupita patsogolo

YACHOKERA PA TSAMBA 16

Association (COSANA), Fast5, Commonwealth Games Netball World Championship.

Timu yathuyi inayamba kutenga nawo mbali mu mpikisano wamasewero a dziko lonse mchaka cha 1995 ku England.

Mu mpikisano wadziko lonse wa Netball World Championships mchaka cha 2007, timu ya Malawi inali yachisanu kupambana itachita bwino kuposa matimu amphamvu ngati Wales, Cooks Islands, ndi South Africa.

Chipambano chachikulu cha timu ya Malawi pa masewerowa chinali pampikisano omwe timuyi inalandira mendulo yamkuwa pa mpikisano wa mchaka cha 2016 wa Fast5 Netball World Series.

Mmbuyomo, mchaka cha 2012, Malawi inapambanapo mpikisano wamayiko onse amu Afirika wa Netball Africa Championship.

Dziko la Malawi lakhalapo ndi akatswiri odziwa bwino masewerowa monga Mary Waya, Peace Kaluwa Chawinga, malemu Emma Mzagada, Linda Magombo mpaka Mwai Kumwenda, Towera Vinkhumbo ndi Joyce Mvula.

Posakhalitsapa dziko lino lawonanso masewero ampira wamiyendo wa atsikana ukupita patsogolo. Kwa nthawi yoyamba timu ya mpira wa miyendo ya atsikana inapereka chimwemwe kwa Amalawi itapambana kukhala akatswiri a COSAFA mchaka cha 2023, itachita bwino modzidzimutsa kumpikisanowu motsogozedwa ndi mphunzitsi, Lovemore Fazili.

Timuyi inapambana mpikisanowu motsogozedwa ndi Temwa Chawinga yemwe pa nthawiyo amakhala ku China komwe amasewera masewerowa.

Masewero ampira wamiyendo wa a atsikana ukupita patsogolo kwambiri mdziko lino.Matimu a mpira wa miyendo wa atsikana akuchuluka ndipo pano kuli matimu monga; Ascent Academy, FCB Nyasa Big Bullets, Mighty Mukuru Wanderers Women komanso Kukoma Ntopwa Girls yomwe inapambana mpikisano wa FAM Women's National Football ndipo inakwanitsa kutenga nawo mbali mu mpikisano woyamba wa COSAFA Women's Football ku South Africa.

Kuyambitsidwa kwa mpikisano wa FAM Goshen women's National Football Championship umene mneneri Shepherd Bushiri anayika ndalama zokwana K 21 million kwathandizira kwambiri kutukula masewerowa.

Dziko lino lasula osewera awiri ochita bwino kwambiri omwe akusewera kumayiko a France komanso United States of America .

Osewerawa ndi atsikana abanja limodzi, Tabitha ndi Temwa Chawinga.

Bungwe lowona zamasewero la CAF likulimbikitsa mayiko kuti matimu a mpira wamiyendo wa anyamata omwe akufuna kutenga nawo mbali m'mipikisano yawo akuyenera kukhala ndi matimu a mpira wamiyendo wa atsikana ndipo izi zidathandiza kuti masewerawa apitebe patsogolo mdziko muno.


*Tiziyang'ana komwe tikuchokera pazamasewero - Charles Nyirenda*

NYUZIPEPALAYI NDI YA ULERE CHONDE MUKAWERENGA PATSANI ANZANU AWERENGEKO

# MASEWERO



Katswiri wamasewero osambira, Chang'anamuno wakonzeka

TSAMBA 15

VOL. 46 NO. 7 | YAULERE | Boma Lathu, Julayi, 2024

WOLEMBA
TIONE ANDSEN



Timu ya mpira wamiyendo ya atsikana ya Malawi, the Scotchers

# Zaka 60 zamasewero ku Malawi

PAMENE dziko la Malawi likhale likukondwerera zaka 60 za ufulu wodzilamulira pa 6 Julayi, 2024, masewero a mpira wa miyendo komanso mpira wa manja wapita patsogolo poyerekeza ndi mmene zinaliri mzaka zammbuyomu.

Mpira wa miyendo umene ndi otchuka kwambiri kuno ku Malawi uli ndi matimu oyimira dziko lino atatu omwe ndi a achinyamata osakwana zaka 17, 20, 23 komanso timu ya mpira wamiyendo yadziko lino yomwe imadziwika kuti Flames.

Pamene tikukwanitsa zaka 60 zi, matimuwa pano ndi okhazikika ndipo amathandizira kwambiri kupeza akatswiri osewera mtimu yayikulu ya dziko lino.

Chipambano chachikulu cha timu yadziko lino chinali mchaka cha 1987 pamene timu yathu inachita bwino kukhala yachitatu pomaliza pa masewero ampira wamiyendo wa mayiko onse amu Afirika umene unachitikira mdziko la Kenya motsogozedwa ndi malemu Reuben Malola.

Timu ya Malawi inapambanapo katatu mu mipikisano ya mchigawo cha ku mmawa ndi pakati pa Afirika (Confederation of East and Central Africa Football Association (CECAFA)) mzaka zapakati pa 1978, 1979 ndi 1988.

Timu ya Malawi inakwanitsapo kupita kumpikisano wa mayiko onse amu Afirika wa Africa Cup of Nations (AFCON) ku Ivory Coast mchaka cha 1984, ku Angola mchaka cha 2010 komanso ku Cameroon mu 2021.

M'maulendo onse atatuwa. timu ya dziko linoyi inali ndi aphunzitsi akwathu konkuno monga Henry Moyo, Kinnah Phiri ndi Meke Mwase.

Mu mipikisanoyi, timu yathu sinachite bwino kwenikweni kupatula mchaka cha 2021pamene timuyi inalimbikira ndikukwanitsa kufika gawo lachiwiri lampikisanowu pomwe inagonja ndi Morocco ndizigoli ziwiri kwa chimodzi.

Panali patadutsa zaka 26 kuti Malawi itenge nawo gawo mundime yomaliza ya AFCON ku Angola mu 2010 komanso panadutsa zaka 11 kuti ipite nawo kumpikisanowu ku Cameroon mu 2021.

Timu ya Malawi sinapambanepo mu mpikisano wa COSAFA kuyambira pomwe mpikisanowu unakhazikitsidwa mchaka cha 1997 koma yakwanitsapo kufika mundime yomaliza kawiri mu 2001 ndi 2002.

Katswiri onenapo pankhani zamasewero ampira wamiyendo, Charles Nyirenda anati vuto la timu ya Malawi lagona pamalingaliro ofuna kupeza zotsatira mwachangu.

“Timafuna tipeze zotsatira lero tisanafufuze mmene takhala tikuchitira mmbuyo posaganiziranso za mawa. Tikuyenera kusiya kuganiza zopambana lero koma tiganizire za mmene tingakonzere mavuto athu kuti mawa tipambane.

“Mukayang'ana m'mbuyomu, mphunzitsi wa timu ya dziko lino, John Kaputa, anatenga timu ya anthu a zaka zosapitirira 20 kupita mdziko la Ghana mchaka cha 1999, ndipo timuyi ndi imene inawonetsa chamuna posewera mmipikisano ina yambiri ya achinyamata ndipo anatitsogolera mu Mpikisano wa Africa Cup of Nations mchaka cha 2010,” anatero Nyirenda.

Kupatulapo mpira wa miyendo, masewera ena omwe asangalatsa anthu mdziko muno ndikuwonetsa chipambano ndi timu ya dziko ya mpira wa manja ya atsikana yomwe kwa nthawi yayitali yakhala ikutchuka ndikupambana kwake.

Timu ya dziko linoyi yomwe pano ili pa nambala 6 padziko lonse lapansi yathandizira kwambiri kudziwika kwa dziko lino kumayiko akunja. Timuyi yakwanitsa kupambanapo mu mipikisano ya African Netball Championship, Confederation of Southern African Netball

TSAMBA 15